9. Njira yoyamba ndi yakuti, Ife tidzamukonda. Njira yachiŵiri ndi yakuti: Tidzamumvera. Kutereku kumatanthauza kuti tidzatsatira Yesu. Ife tizichita zinthu zimene Iye amanena. Tidzapita kumene Yesu akufuna kuti tipite. Pamene Yesu anaitana asodzi anayi a nsomba, Petro, Andreya Yohane ndi Yakobo, iwo anamutsata Iye. Iwo anamumvera Iye. Kumvera kumatanthauza zinthu zambiri.

Mateyu 4:20:
    Ndipo iwo anasiya pomwepo makokawo, namtsata Iye.

Pa ndime iyi, kodi ophunzira anachita chiyani pomumvera ndi kumtsatira Yesu?

___________________________________________

===========================================================

10. Iwo anasiya makoka awo. Zimenezi zimatanthauza kusiya ntchito zawo zakale. Iwo anatsata Yesu. Izi zimatanthauza kuti anasiya mabanja awo nthaŵi zina. Akuphunzira sanakankhire ntchito yawo kutsogolo kwa Yesu. Iwo sanatenge mabanja kapena abwenzi awo kukhala oyamba mmalo mwa Yesu miyoyo mwawo. Pamene Yesu anaŵaitana iwo anasiya zilizonse ndi kumvera Iye.

Mateyu 16:24:
    pomwepo Yesu anati kwa ophunzira ake, "Ngati munthu afuna kudza pambuyo panga, adzikane yekha natenge mtanda wake nanditsate Ine."

Ndime imeneyi ili kunena kuti ophunzira ayenera kudzikana yekha ndi kusenza mtanda wake. Kodi china ndi chiyani chimene ndimeyi ikunena kuti iye achite pomvera Yesu?

___________________________________________

===========================================================

11. Ndimeyi imanena kuti titsatire Yesu. Kutsata kumatanthauza kumvera. Kumatanthauza kuchita zimene Yesu amanena. Yesu anapeza Mateyu (kapena Levi) pa ntchito yake. Iye anali kukhometsa misonkho. Pa nthawi imeneyo okhometsa misonkho anali anthu olemera. Mateyu anasiya chuma chake natsata Yesu.

Munthu wina wachuma ndipo anali woweruza nthaŵi zina anafunsa Yesu mmene angalandirire moyo wosatha. Yesu anamuuza kuti agulitse zonse zimene anali nazo ndi kumutsata Iye. Munthuyo anachoka napita ali wolunda. Iye anakonda chuma chake kwambiri. Iye sanali kufuna kumvera Yesu

Kodi ife tikhoza kumvera Yesu monga ophunzira woona ngati titamaika chuma mmiyoyo yathu kukhala choyamba?

____________________________

================================================================

12. Ife sitingamvere ngati titaika chuma kukhala choyamba. Sitiyenera kuika mabanja athu kukhala oyamba. Samueli si Mkhristu. Iye anafuna kutsatira Khristu. Koma iye anali kuopa makolo ake. Iye anadziŵa kuti iwo adzakhala okwiya ngati iye akhala ophunzira wa Yesu.

Mariya nayenso anali wamantha. Kwa miyezi yambiri iye anaganizira zokhala Mkhristu. Iye anati, "Ngati ine nditsatira Yesu, abwenzi anga adzandiseka. Koma tsiku lina iye anati, "Ine ndisoŵa Yesu koposa mmene ndisoŵera abwenzi anga. Ine ndimtsatira Iye." Potsiriza pake abwenzi ake nawonso anakhala Akhristu.

Ngati ife tikhala ophunzira woona, kodi timamvera yani? ____________

================================================================

13. Ife timamvera Yesu. Iye ndi amene amatiuza zoyenera kuchita. Ife tiyenera kuyamba kumutsata ndipo timayenera kupitiriza kumutsatabe.

Yohane 8:31:

Chifukwa chake Yesu ananena kwa Ayuda aja adakhulupirira Iye, "Ngati mukhala inu m'mawu anga (kapena kupitiriza kumverabe) muli akuphunzira anga ndithu."

Monga ophunzira a Yesu poyamba tidzamkonda Iye. Ndipo tidzachita chiyani ndi Mawu ake?

____________________________________________

================================================================

14. Ife tidzapitiriza kukhala m'mawu ake kapena kumvera Iye. Nthaŵi zina kumakhala kovuta kuchita zimenezi. Ambiri a ophunzira ake anaphedwa chifukwa chomvera Yesu. Yohane anakhala ndi moyo kufikira anakalamba. Koma iye anachotsedwa nakamuika pachisumbu payekha. Chidatengera ophunzira mtengo wapatali kwambiri kutsatira Ambuye.

Kodi ife monga ophunzira woona tidzachita chiyani potsata Yesu?

(1) ________________________________________

(2) Ife tidzamvera Iye.

==================================================================

15. Ife tidzamkonda Iye. Pamene tikonda Yesu, chidzatithandiza ife. Timafuna kukhala monga Iye. Timafuna kukhala ophunzira ake.

Kodi ife monga ophunzira woona tidzachita chiyani kwa Yesu?

(1) Ife tidzamukonda Iye

(2) ________________________________________

==================================================================

16. Ife tidzamumvera Iye. Anthu ena amadzitcha okha Akhristu. Koma sachita zinthu monga Akhristu. Iwo amatsatira Yesu kufikira wina ataŵaseka iwo. Kapena iwo amatsata pokhapokha atachotsedwa ntchito yawo chifukwa chakukhala Akhristu. Kapena iwo amatsata chifukwa chakuti wina wanena kuti, "ndidzakutsekerani m'ndende chifukwa chokhala Mkhristu."

Kodi anthu ameneŵa ndi ophunzira oona? ____________________________

Kodi inu nthaŵi zina mumaona ngati kuti simuli ophunzira oona? _______

Tengani nthaŵi kuti muganizire za phunziro lalero. Konzani ulaliki kuti mudzithandize ndi kuthandizanso anthu. Papepala lina lembani zinthu zimene mungakanene. Mubweretse pepala lanu ku kalasi. Lalikirani ulalikiwo mwansanga monga mungathere.

==================================================================

17. Kuchokera pa zinthu zimene Yesu ananena za ophunzira, kodi ife monga akuphunzira oona tingachite bwanji potsatira Yesu?

(1) ______________________________________________________

(2) ______________________________________________________

SABATA LACHISANU NDI CHIMODZI: KHRISTU NDI AKUPHUNZIRA AKE
·TSIKU LACHITATU: IYE AMAPANGA OPHUNZIRA AKE KUKHALA ASODZI A ANTHU

1. Chinthu chachikulu chimodzi chomwe Yesu anachita chinali kuphunzitsa akuphunzira. Iye anatenga nthaŵi yaikulu ali kuŵaphunzitsa. Iye anali kuŵafotokozera tanthauzo lake la kukhala ophunzira oonadi.

Kuchokera ku zinthu zimene Yesu ananena za ophunzira, kodi ife monga ophunzira oonadi tidzachita bwanji pomutsata Iye?

(1) ______________________________

(2) ______________________________

==========================================================

2. Ife tidzamukonda Iye ndipo tidzamumvera Iye. Taona kuti Yesu anagwirira ntchito ophunzira ake. Iye anaŵatcha iwo kuti atumwi. "Atumwi" amatanthauza "Otumidwa." Yesu anafuna kuti ophunzira apite ndi kukauza anthu za iye. Iye anafuna kuti akhale "asodzi a anthu." Lero tiphunzira za zimenezi.

| |
|---|
| Mu Mateyu 4:19 Yesu anati, "Tiyeni pambuyo panga, ndidzakusandutsani asodzi a anthu."<br>(1) Amene amauza anthu za Yesu<br>(2) Amene amathandiza anthu kuti alandire Yesu. |

Tsopano tengani Buku Lopatulika ndi kuŵerenga Mateyu 4:18 mpaka 22. Lembani mzere pansi pa ndime 19 ndipo musiye Buku Lopatulika lili lotsegula.

==========================================================

3. Pa ndime zimenezi Yesu anali kuitana ena a mwa ophunzira ake. Tikuona kuti asodzi ansomba anasiya zinthu zonse natsata Yesu. Iwo anasiya ntchito yawo. Iwo anasiya nyumba zawo. Masiku anonso anthu amasiya zinthu zawo ndi kutsatira Yesu. Ena amasiya ntchito yawo yakale. Ena amasiya mabanja awo kapena abwenzi awo. Ena amasiya chipembedzo chawo chakale. Iwo amamva Khristu ali kuitana.

Mateyu 4:19:

Yesu anati, "Tiyeni pambuyo panga, ndidzakusandutsani asodzi a anthu."

Kodi Yesu analonjeza kanthu kena kwa ophunzira pa ndime imeneyi?

____________________________________________

==========================================================================

4. Inde, Iye analonjeza kuŵasandutsa kanthu kena. Iye analonjeza kuti iwo "azisodzera" anthu kwa Yesu. Andreya anauza mbale wake, Petro, za Yesu. Filipo anauza bwenzi lake, Nataniyeli (kapena Batolomeyo). Anthu onseŵa anakhala ophunzira ake a Yesu.

Kodi Yesu anaŵatcha chiyani ophunzira amene anali "kusodzera" anthu ena kwa Iye?

________________________________________________________

==========================================================================

5. Iye anali kuŵatcha "asodzi a anthu." Petro ndi Andreya, Yakobo ndi Yohane anamvetsetsa kuti zimenezi zinatanthauza chiyani. Iwo anali asodzi a anthu. Iwo anazolowera kusodza nsomba Tsopano iwo azisodza anthu. Yesu sanagwiritse ntchito Mawu ameneŵa ndi ophunzira ena asanu ndi atatuwo. Koma Iye anaŵauza kuti iwo adzakhala mboni zake. Mboni imanena zimene ili kudziŵa. Akuphunzira adakamanena zimene anadziŵa za Yesu. Iwo adakamathandiza anthu kuti alandire Yesu. Kumeneku ndiko kutanthauza kwake kwa kukhala msodzi wa anthu.

Mateyu 4÷19:
Yesu anati, "Tiyeni pambuyo panga, ndidzakusandutsani asodzi a anthu."

Yang'ananinso pa ndimeyi. Kodi ophunzira amayenera kuchita chiyani kwa Yesu mmalo mwakuti akhale asodzi a anthu?

______________________________

____________________________________________________________________

==========================================================================

6. Iwo anayenera kumutsata Iye. Ndipo anayenera kusodza anthu. Iwo anayenera kuuza anthu za Yesu. Iwo anayenera kuthandiza anthu kuti alandire Yesu. Ngati inu mukonda Yesu ndi kumumvera Iye mudzauza ena za Iye. Ena a iwo amene mudzaŵauza adzamulandira Iye.

Kodi ndi ndime iti imene imanena kuti, "Tiyeni pambuyo panga, ndidzaku-sandutsani asodzi a anthu?" Ngati muli kukaikira, yang'anani m'Buku Lopatulika.

_______________

_______________

==========

7. Ndimeyi ndi Mateyu 4:19. Ndime imeneyi ndi yofunika chifukwa ndi Mawu a Yesu. Ndiyofunika chifukwa imatiuza zomwe Iye anafuna kuti ife tizichita. Ndiyofunika chifukwa imatiuza mmene Yesu angatisandutsire.

Mateyu 4:19:
"Tsatani pambuyo panga, ndidzakusandutsani asodzi a anthu."

Tsopano loŵezani ndime imeneyi. Pamene mungainene mosaoneranso pa buku ilembeni ndimeyi apa.

_______________

_______________

==========

8. Yesu amafuna kutisandutsa ife kukhala asodzi a anthu. Koma kodi msodzi wa anthu ndi ndani? Iye amakhala zinthu ziŵiri.

(1) Amene amauza anthu za Yesu.
(2) Amene amathandiza anthu kuti alandire Yesu.

Ife timalankhula kwa anthu zinthu zambiri. Timagwira ntchito za mitundu yosiyanasiyana. Koma ntchito yofunika koposa ndi yosodzera anthu kwa Yesu.

Kodi Yesu amafuna ndani kuti akhale asodzi a anthu? _______________

==========

9. Iye amafuna kuti ife tikhale asodzi. Iye amafuna ophunzira ake kukhala asodzi. Pamene ife tisodzera anthu kwa Khristu timakhala monga mtengo wa zipatso.

Yohane 15:8:

Mwa ichi alemekezedwe Atate wanga, kuti mubale chipatso chambiri, ndipo mudzakhala akuphunzira anga.

Kodi ife tikhoza kudziŵitsa anthu ena za Yesu motani? ______________

______________________________________________________________

==================================================================

10. Ife tikhoza kuwauza iwo. Iwo sangamve za Yesu pokhapokha wina wake ataŵauza iwo. Ifeyo tiyenera kuchita zimenezi. Pamene tichita zimenezi ena mwa iwo adzasodzedwa. Iwo adzatsatiranso Yesu.

Yohane 15:16:

Inu simunandisankha Ine, koma Ine ndinakusankhani inu, ndipo ndinakuikani, kuti mukamuke inu ndi kubala chipatso, ndi kuti chipatso chanu chikhale; kuti chimene chilichonse mukapemphe Atate m'dzina langa akakupatseni inu.

Mwina inu munadzala mtengo wa mango. Kodi ndi chifukwa chiyani munabzala? Ndi chifukwa chakuti muli kufuna mango ena ambiri. Kodi ndi chifukwa chiyani Ambuye anabzala Akhristu m'malo ena? Ndi chifukwa chakuti iye anafuna Akhristu ambiri kuchokera mmalo amenewo.

Kodi Yesu amatcha ndani ophunzira amene amauza anthu za Iye?

______________________________________________________________

==================================================================

11. Iye amaŵatcha asodzi a anthu. Iye amaŵathandiza kuti asodze anthu a Mulungu. Iye amaŵathandiza kuti akhale ndi zipatso m'miyoyo yawo.

Agalatiya 5:22-23:

Koma chipatso cha Mzimu ndicho chikondi, chimwemwe, mtendere, kuleza mtima, chifundo, kukoma mtima, chikhulupiriro, chifatso, chiletso.

Yesu amaika zinthu zabwino zimenezi m'miyoyo yathu kupyolera mwa Mzimu Woyera. Anthu ena amaona zinthu zabwino zimenezi. Iwo amazifunanso. Koma ndizosakwanira kungokhala ndi zinthu zabwino m'miyoyo mwathu. Anthu amayenera kudziŵa komwe zinthu zabwinozi zimachokera.

Kodi ife timayenera kuchita chiyani kwa anthu kuti iwo adziŵe za Yesu?

_______________________________________________

===========================================================================

12. Timayenera kuŵauza iwo za Yesu. Ngati ife tili ophunziradi woona, anthu adzaona zinthu zabwino m'miyoyo mwathu. Iwo adzafuna kudziŵa za zimenezo. Ife tidzaŵauza kuti ndi ndani amene anatisintha ife.

Dzina lakuti Petro limatanthauza kuti "thanthwe." Pachiyambi Petro anali monga mchenga. Iye anali kunena zinthu zosasamala. Iye anakana Yesu katatu chifukwa anali kuchita mantha. Koma patapita nthaŵi iye anakhala wolimba. Iye anakhala monga mwala. Iye anakhala msodzi wa anthu monga momwe Yesu analonjezera.

Kodi msodzi a anthu ndi ndani? _______________________

(1) _______________________________________

(2) Amene amathandiza anthu kuti alandire Yesu.

===========================================================================

13. Msodzi wa anthu ndi amene poyamba amauza anthu za Yesu. Ife timayenera kuthandiza anthu kuti azimvetsetsa chiphunzitso cha Yesu. Anthu ena samadziŵa mmene angalandirire Yesu.

Yesu anaonetsa kuti ophunzira ake akhoza kuthandiza ndi chimenechi.

1 Yohane 13:20:

> Indetu, indetu, ndinena ndi inu, Iye wolandira amene aliyense ndimtuma, andilandire Ine; koma wolandira Ine alandira wonditumа Ine.

Anthu amamva za Yesu koma amayenera kuchitanso kanthu. Asodzi a anthu amayenera kuŵathandiza. Koma tiyenera kuwathandiza kuti achite chiyani kwa Yesu?

_______________________________________________

===========================================================================

14. Tiyenera kuwathandiza kuti amulandire Iye. Imeneyi ndi ntchito ya asodzi a anthu. Kumeneku ndi kutanthauza kwake kwa kusodzera anthu kwa Yesu. Zimenezi ndi zimene Yesu amafuna kuti ife tizichita.

Kodi Yesu anati chiyani pa Mateyu 4:19: ______________________________

____________________________________________________________

===========================================================

15. Iye anati, "Tsatani pambuyo panga, ndidzakusandutsani asodzi a anthu." Msodzi wa anthu ndi wa zinthu ziŵiri. Iye amauza anthu za Yesu.

Kodi china ndi chiyani chimene msodzi wa anthu ali? ______________

____________________________________________________________

===========================================================

16. Msodzi wa anthu ndi amene amathandiza anthu kuti alandire Yesu. Koma anthu ambiri sadziŵa za Yesu. Alipo anthu ambiri otizungulira amene samvetsetsa. Iwo sadziŵa zimene Yesu amaŵachitira. Iwo sadziŵa mmene angamulandirire Iye.

(1) ______________________________________________

(2) Amene amathandiza anthu kuti alandire Yesu.

===========================================================

17. Msodzi wa anthu ndi amene amauza anthu za Yesu. Koma ndikosakwanira kwa anthu kuti angodziŵa za Yesu. Ndikosakwanira kwa iwo kungomvetsetsa. Iwo ayenera kuchita kanthu kena.

Kodi msodzi wa anthu ndi ndani?

(1) Amene amauza anthu za Yesu

(2) ______________________________________________

===========================================================

18. Msodzi wa anthu ndi amene amauza anthu za Yesu ndi kuthandiza anthu kuti alandire Yesu. Mwina inu muli kufuna kukhala msodzi wa anthu. Koma muli kuchita mantha. Kumbukirani kuti Yesu analonjeza kukusandu-

tsani inu kukhala msodzi. Iye akhoza kukupatsani mawu oyenera kuŵanena.

Tsopano weramitsani mutu wanu ndi kupempha Yesu kuti akuthandizeni. Pempherani mawu otere: "Ambuye Yesu, chonde pangeni ine kukhala msodzi wa anthu. Thandizeni kuti ndiuze abwenzi anga za inu. Patseni mawu oyenera kuŵanena. Konzani mitima yawo kuti akulandireni inu. Zikomo, Amen."

==========================================================================

19. Kodi Yesu ananena chiyani pa Mateyu 4:19?

______________________________________________________________________

Kodi msodzi wa anthu ndi ndani?

(1) ____________________________________________________________

(2) ____________________________________________________________

==========================================================================

SABATA LACHISANU NDI CHIMODZI: KHRISTU NDI OPHUNZIRA AKE
TSIKU LACHINAYI: KHRISTU ANALI KUDZUDZULA OPHUNZIRA AKE PAMENE ANACHITA ZOLAKWA

1. Sabata ino tikuphunzira za akuphunzira. Taphunzira kale kuti Yesu anasankha ophunzira apadera khumi ndi aŵiri. Koma Iye amafuna kuti tonsefe tikhale akuphunzira ake. Iye amafuna kuti tizimukonda ndi kumumvera Iye. Pali zinthu zinanso zimene Iye amafuna kuti tizizichita.

Kodi Yesu ananena chiyani pa Mateyu 4:19: ____________________

____________________________________________

Kodi msodzi wa anthu ndani?

(1) ____________________

(2) ____________________

==========================================================================

2. Yesu anati, "Tiyeni pambuyo panga, ndidzakusandutsani asodzi a anthu Msodzi wa anthu ndi amene amauza anthu za Yesu ndi kuwathandiza iwo kuti alandire Yesu.

Yesu anasankha ophunzira ake khumi ndi aŵiri mosamalitsa bwino. Anthu ambiri anali kumutsata Iye. Koma Iye anali kufuna amene akanakhoza kupitiriza ntchito yake. Iye anapemphera usiku wonse asanayambe kuŵasankha. Ophunzira khumi ndi aŵiriwo anali anthu abwino, koma iwo sanali wolungama. Yesu anayenera kuŵaphunzitsa iwo. Lero tiphunzira zinthu ziŵiri za ophunzira.

(1) Yesu anali kudzudzula ophunzira akachita zolakwa.
(2) Pamene Yesu amatidzudzula amafuna kuti ife titembenuke kuchoka ku uchimo athu.

Tsopano tengani Buku Lopatulika ndi kuwerenga zimene akuphunzira anachita. Werengani Marko 9:33-35. Kodi akuphunzira anali kuchita zabwino pa nthaŵi imeneyi?

____________________

==========================================================================

3. Iwo sanali kuchita zabwino. Iwo anali kukangana. Iwo anali kuonetsa kunyada. Anthu ameneŵa anali akuphunzira oonadi. Koma anali kuchita zoipa. Yesu anayenera kuŵadzudzula iwo. Kudzudzula ndiko kuone-

tsa wina wake tchimo lake.

Ophunzira woona akhoza kuchimwa koma Iye sadzapitirizabe kuchita chinthu chomwecho. Iye sadzikonda khalidwe la uchimo. Iye adzamva chisoni ndipo adzatembenuka kuchoka ku uchimo wake.

Kodi Yesu anadzudzula ayani atalakwa? ______________________________

________________________________________________________________

================================================================

4. Yesu anadzudzula ophunzira. Iwo anali womutsatira okhulupirika. Koma iwo nthaŵi zina anali kuchita zolakwa. Yesu sanali kuyang'ana mbali ina pamene iwo anachita zimenezi. Iye sananene kuti, "Palibe kanthu." Iye anali kuvutika. Iye anadzudzula ophunzira ake.

Yakobo ndi Yohane anayenera kuphunzira chifatso ndi chikhululukiro. Yesu anaŵatcha kuti ndi "ana a bingu." Mwina iwo anali kupsa mtima mwa msanga. Taonani zimene zinaoneka tsiku lina.

Luka 9:53-55:

> Ndipo iwo sanamlandire Iye, chifukwa nkhope yake inali yoloza kunka ku Yerusalemu. Ndipo pamene ophunzira ake Yakobo ndi Yohane anaona, anati, "Ambuye, kodi mufuna kuti ife tiuze moto utsike kumwamba ndi kuŵanyeketsa (kapena kuŵapsereza iwo) koma Iye anapotoloka naŵadzudzula.

Kodi ndi pa nthaŵi iti imene Yesu anadzudzula ophunzira ake?

________________________________________________________________

================================================================

5. Iye anaŵadzudzula pamene anachita zolakwa. Iye anaŵaonetsa kuti zimene iwo anali kuchita sizinali kukondweretsa Mulungu. Iye amatidzudzulanso ife. Ife timaŵamva Mawu ake m'mitima mwathu. Timadziŵa kuti tachita zolakwa.

Marko 9:38:

> Yohane anati kwa Iye, "Mphunzitsi, taona munthu alikutulutsa ziŵanda m'dzina lanu; ndipo tinamletsa, chifukwa sanali kutsata ife; koma Yesu anati, "Musamamletsa iye; pakuti palibe munthu adzachita cha mphamvu m'dzina langa, nadzakhoza msanga kundinenera Ine zoipa."

6. Yesu amachita zimenezi. Nthaŵi zina Iye amalankhula m'mitima mwathu. Nthaŵi zina Iye amagwiritsa ntchito Akhristu ena kutionetsa ife zimene zili zolakwika. Ena mwina amatiŵeruza molakwa; koma nthaŵi zambiri iwo amakhala olondola pa zimene anena. Yesu anaphunzitsa ophunzira ake za zimenezi.

Luka 17:3:

Kadzichenjerani nokha, akachimwa mbale wako umdzudzule, akalapa umukhululukire.

Kodi Yesu anachita chiyani pamene ophunzira ake anachita zolakwa?

---

==========================================================================

7. Iye amaŵadzudzula iwo. Iye anaŵaonetsa kuti iwo anali olakwa. Koma timayenera kukhala wossamala pamene tili kudzudzula ena. Tsiku lina ophunziraŵa anayesa zimenezi.

Marko 10:13-14:

Ndipo analinkudza nato kwa Iye tiana, kuti akatikhudze; ndipo ophunzirawo anaŵadzudzula. Koma pamene Yesu anaona anakwiya, ndipo anati kwa iwo, "Lolani tinana tidze kwa Ine, musatiretse; pakuti ufumu wa Mulungu uli wa totere."

Kodi ndi cholakwa chotani chimene akuphunzira anachita pano?

---

==========================================================================

8. Iwo anadzudzula anthu ali kubweretsa ana. Poyamba iwo sanathe kuona zimene Yesu anafuna. Iwo anagwiritsa ntchito njira yawo ya kaweruzidwe. Iwo anachita zolakwa.

Pachiyambi cha phunziro ili tawerenga mmene akuphunzira anali kukanganirana. Iwo anali kukangana za kuti kodi ndi ndani amene adzakhale wamkulu . Ndipo Yesu anati ngati wina aliyense afuna kukhala wamkulu iye ayenera kukhala otumikira onse. Akuphunzira anachita zolakwa pomakangana zakuti wamkulu ndi ndani.

Kodi Yesu anali kuchita chiyani pamene ophunzira anachita zolakwa?

---

==========================================================================

9. Iye anali kuŵadzudzula iwo. Iye amatidzudzulabe ife monga ophunzira ake. Pamene Iye ali kutidzudzula ife Iye amayembekeza kuti ife titembenuke kuchokera ku uchimo wathu. Petro anali wophunzira woonadi. Koma iye anali kuchita zinthu zoipa. Usiku wina iye anayamba kuyenda pa mwamba pa madzi pomatsata Yesu. Izi sizinali zoipa. Koma pamene Iye anaona mphepo anachita mantha nayamba kumira. Iye anapfuula, "Ambuye pulumutseni." Yesu anamudzudzula chifukwa cha chikhulupiriro chaching'ono.

Mateyu 14:31:

> Ndipo pomwepo Yesu anatansa dzanja lake, nangwira iye, nanena naye, "Iwe wokhulupirira pang'ono, wakayikiranji mtima?"

Kodi Yesu anafuna kuti Petro apitirizebe ndi kukaika? ______________

==========================================================================

10. Yesu anafuna kuti Petro atembenuke kuchokera ku chikaiko chake. Panalinso nthaŵi ina yomwe Yesu anadzudzula Petro chifukwa cha tchimo lake. Tsiku lina Yesu anauza ophunzira ake kuti adzavutika ndi kudzafa.

Mateyu 16:22-23:

> Ndipo Petro anamtenga Iye, nayamba kumdzudzula, kuti "Dzichitireni chifundo Ambuye." Sichidzatero kwa inu ayi," koma Iye anapotoloka, nati kwa Petro, "Pita kumbuyo kwanga, Satana iwe; ndiwe chondikhumudwitsa Ine; chifukwa sumasamalira za Mulungu, koma za anthu."

Pamene Yesu ali kutidzudzula ife, kodi Iye amafuna kuti titembenuke kuchokera ku chiyani?

________________________________________

==========================================================================

11. Iye amafuna kuti ife tizitembenuka kuchokera ku machimo athu. Iye amayembekeza kuti ife tiziŵasiya machimowo. Iye amayembekeza kuti tizichita zabwino mmalo mochita zolakwa. Pamene Yesu anali pafupi kufa, asilikali anabwera kudzamugwira. Petro anali pamenepo. Iye anaganiza kuti akhoza kuteteza Yesu.

Luka 22:50-51:

> Ndipo wina wa iwo (Petro) anakantha kapolo wamkulu wa ansembe nadula khutu lake lamanja. Koma Yesu anayankha nati, "Lolani kufikira kumene."

Kodi ndi ndani amafuna kuti ife titembenuke kuchokera kumachimo athu Iye akatidzudzula?

_______________________________________________

================================================================

12. Yesu ndiye amafuna zimenezi. Ichi ndicho chifukwa chake amatidzudzulira ife. Iye amafuna kuti atithandize ife. Iye amafuna kutipanga ife ophunzira bwino. Petro anali ndi zinthu zambiri zoyenera kuziphunzira. Iye amaganiza kuti ndi wamphamvu koposa momwe analiri. Iye anauza Yesu kuti ngakhale kukafa naye, sadzamukana. Koma usiku omwewo iye anati sanamudziŵe Yesu. Iye anachita zimenezi katatu. Koma chimenechi chinakwiyitsa Petro kwambiri. Iye anapita kunja nakalira. Petro anamva manyazi ndi chisoni pamene iye anachimwa. Iye anali wophunzira woonadi.

Pamene Yesu amatidzudzula ife monga ophunzira, kodi iye amafuna kuti tizichita chiyani ndi machimo athu?

_______________________________

================================================================

13. Iye amafuna kuti titembenuke kuchokera kumachimowo. Mmodzi wa ophunzira sanatembenuke kuchoka ku machimo ake pa nthaŵi yomweyo. Yudasi amatanthauza "kulemekeza" koma panalibe amene analemekeza Yudasi. Yudasi nkutheka kuti poyamba anali wophunzira woona. Koma iye anakohda ndalama. Iye anayamba kukonda ndalama koposa monga momwe akadakondera Yesu. Iye anali kumaba ndalama zimene anali kuzisunga. Ndipo iye anapereka Yesu chifukwa cha ndalama. Pamene Yesu anapachikidwa, Yudasi anamva chisoni. Koma iye sanatembenuke kuchokera ku uchimo wake ndikuti atsate njira yolondora. Mmalo mwake anadzipha yekha. Ife sitimayenera kutsata chitsanzo chake.

Kodi Yesu anali kuchita chiyani kwa ophunzira ake akalakwa?

_______________________________________________________________

================================================================

14. Yesu anali kudzudzula ophunzira pamene achita zolakwa. Ambuye anasankha anthu wamba kuti akhale ophunzira ake. Iwo anali ofooka. Iwo anali kuchita zolakwa. .Iwo anali kuchimwa. Koma pamene iwo anali kuchita zolakwa iye anali kuŵadzudzula. Mmenemu ndi mmene iwo anaphunzirira kukhala ophunzira abwino. Iwo anaphunzira kuti Yesu anali kuŵachotsa mmachimo.

Pamene Yesu amatiazuazula ife monga akuphunzira, kodi Iye amafuna kuti ife tizichita chiyani?

______________________________

______________________________

==========================================

15. Iye amafuna kuti ife titembenuke kuchokera ku machimo athu. Apa pali anthu ena amene akuti ndi ophunzira. Lembani kuti <u>Inde</u> pambali pa amene ali wophunzira woonadi. Lembani <u>Ayi</u> pambali pa amene sali wophunzira woonadi.

______ Enoki amachimwa ndipo amabisa machimo ake. Iye amafuna kuti anthu azimuganizira kuti ndi Mkhristu wabwino.

______ Sani amavomereza pamene Iye achita molakwa ndi kupempha Akhristu amupempherere.

______ Davide amababe ndalama, koma zimakhala zochepa pa nthaŵi imodzi.

______ Yakobo samabvutika ndi mawu oipa ndi nkhani za wamba pokha pokha Akhristu akakhala pafupi.

______ Idi amayesedwa kuti abe. Koma pamene alephera amabwezera chinthu chakubacho amanena kuti ali ndi chisoni.

______ Pamene anthu anena zinthu zankhanza kwa Amosi; iye amalankhula mofatsa ndi chikondi. Koma iye amadana naobe mumtima mwake.

==========================================

16. Tidzakambirana za izi m'kalasi.

Kodi Yesu anali kuchita chiyani pamene ophunzira ake akalakwa?

______________________________

Pamene Yesu atidzudzula ife monga ophunzira, kodi Iye amafuna kuti ife tichite chiyani?

______________________________

______________________________

==========================================

SABATA LACHISANU NDI CHIMODZI: KHRISTU NDI OPHUNZIRA AKE.
TSIKU LACHISANU: KUBWEREZA

Takhala tili kuphunzira ntchito zoyamba za Yesu kwa masabata atatu. Pa i zina zambiri zoyenera kuphunzira. Koma mwachita kale zambiri. Mwaona mmene Yesu anayambira kuchita zozizwitsa. Mwaona chikondi chake chachikulu ndi mphamvu yake. Mwaonanso mmene Iye anapangira akuphunzira ake.

Musanapitirize, tiyeni tibwereze zomwe mwaziphunzira. Yesetsani kuyankha funso lililonse mphunziro limeneli. Musayang'anenso m'mbuyo mwa buku lanu kufikira mutalemba yankho pa mzere uliwonse. Pamene mwatsiriza kulemba, bwereraninso kuti mukapeze mayankho. Ngati yankho lanu lili lolakwa, lipheni ndi mzere. Ndipo lembani lolondola pamwamba pake.

MAFUNSO OCHOKERA PA SABATA LACHINAYI:

1. Kodi ndi zinthu zazikulu zotani zimene Yesu anachita nthaŵi ya moyo wake zimene zinaonetsa kuti Iye ndi Mwana wa Mulungu?

______________________________

2. Kodi chozizwitsa choyamba cha Yesu chinali chitani? ____________

______________________________

3. Kodi chozizwitsa choyamba cha Yesu chinapangitsa akuphunzira kupanga chiyani?

______________________________

______________________________

4. Pa Yohane 3, kodi Yesu anati ndi chiyani chimayenera kuoneka kwa ife tisanaloŵe mu ufumu wa Mulungu?

______________________________

______________________________

5. Kuchokera ku mawu a Yesu a kwa Nikodemo, kodi ndi chiyani chimaoneka kwa ife pa kubadwanso mwatsopano?

______________________________

______________________________

6. Kuchokera ku mawu a Yesu kwa Nikodemo, kodi ndi ndani amalandira kubadwa kwatsopano ndi moyo watsopano?

______________________

Kodi chidzaoneka nchiyani kwa iwo amene sakhulupirira? __________

__________________________________________________

7. Kodi Yesu poyamba analankhula kwa ndani mu Samariya? __________

__________________________________________________

Kodi Yesu anautcha chiyani moyo wosatha umene Iye anafuna kuupereka kwa Iye?

__________________________________________________

8. Pamene Yesu analalikira ku Nazarete, kodi anthu anachita chiyani?

__________________________________________________

__________________________________________________

Kodi chitsanzo cha Yesu cha ku Nazarete chimatiphunzitsa ife kuchita chiyani pamene anthu akutikana ife?

______________________

__________________________________________________

==================================================================

MAFUNSO OCHOKERA PA SABATA LACHISANU.

9. Kodi timadziŵa kuti Yesu ali ndi mphamvu yoposa ziŵanda motani?

__________________________________________________

Kodi kudziŵa zimenezi kumatithandiza ife kuti Yesu angatichitire chiyani?

__________________________________________

10. Yesu atangotuluka m'Sunagoge ku Kapernao anachita zozizwitsa zitatu zimene zinaonetsa kuti Iye amatisamalira ife.

(1) Kodi Iye anaonetsa motani kuti amasamalira mabanja athu?

______________________________

(2) Kodi Iye anaonetsa motani kuti Iye amasamalira ntchito yathu?

______________________________

(3) Nanga Iye anaonetsa motani kuti amasamalira miyoyo yathu?

______________________________

11. Pamene munthu wodwala manjenje anatsitsidwa kuchokera pa tsindwi, kodi Yesu anachita chiyani chimene chinali chachikulu kuposa kumuchititsa iye?

______________________________

______________________________

12. Kodi ndi gulu liti la Ayuda m'nthaŵi ya Yesu limene limayesa kusunga malamulo ambiri koma sanali kupembedza Mulungu moonadi?

______________________________

13. Kodi timayenera kupembedza Mulungu motani? Yankhani polemba Yohane 4:24.

______________________________

______________________________

14. Kodi ndi tsiku liti limene linali sabata ya Ayuda lopumula ndi kupembedza?

______________________________

N'chifukwa chiyani tsiku lopembedza ndi kupumula la Akhristu linasinthidwa kukhala la Sande?

______________________________

______________________________

Kuchokera m'chiphunzitso cha Yesu, poonjezera kupumula ndi kupembedza, kodi china ndi chiyani chabwino choyenera kuchichita pa Sabata?

______________________________

==================================================

MAFUNSO OCHOKERA SABATA LACHISANU NDI CHIMODZI.

15. Lembani maina asanu ndi limodzi mwa ophunzira khumi ndi aŵiri amene Yesu anaŵatcha kuti atumwi.

(1) ____________________ (4) ____________________

(2) ____________________ (5) ____________________

(3) ____________________ (6) ____________________

16. Kuchokera pa zinthu zimene Yesu ananena za akuphunzira, kodi ife monga ophunzira oonadi tizichita chiyani potsata Yesu?

(1) ________________________________________

(2) ________________________________________

17. Kodi Yesu anati chiyani pa Mateyu 4:19. ____________________

________________________________________

________________________________________

18. Kodi msodzi wa anthu ndi ndani?

(1) ________________________________________

(2) ________________________________________

19. Kodi Yesu anali kuchita chiyani pamene ophunzira ake alakwa?

________________________________________

20. Pamene Yesu ali kudzudzula ife, kodi Iye amafuna kuti tichite chiyani?

________________________________________

________________________________________

==============================================================

Pamene mwadziŵa mayankho onseŵa, pitaninso ku tsamba 79. Bisani mayankho amene mwalemba. Yesani kuyankha mafunso onse.